

KALONDOLONDO PA IMFA ZOBWERA CHIFUKWA CHA UCHEMBERE NDI IMFA ZA MAKANDA

Zoyenera kudziwa:

Ndi ufulu wa mayi wina aliyense kukhala ndi uchembere wabwino. Komanso ana obadwa mdera lathu lino ali ndi ufulu wokhala ndi moyo.



Moyo wa thanzi wa amayi ndi makanda ndi gwero la moyo wapamwamba. Pamene chipatala cha Mkanga (MWC) chikuyembekezera kuyamba kupereka thandidzo la sikelo ya amayi apakati komanso kutsegula maternity, nkofunikira kuti tidziwe za umoyo wa thanzi wa amayi oyembekezera, amene abereka kumene komanso ana akhanda.

Tidzaika mu kaundula zonse zomwe zachitika zokhudza imfa zobwera chifukwa cha uchembere ndi imfa za makanda zomwe zachitika mdela lozungulira chipatala cha Mkanga (MWC). Kutolera nkhani zonsezi zizathandiza chipatala cha Mkanga kupeza njira zomwe zingathandize kupititsa patsogolo chisamaliro ndi chithandizochi.

Pamene mwamva za imfa ya mayi yobwera chifukwa cha uchembere kapena imfa ya khanda, tsatirani izi.

- Fufuzani nkhani yonse yokhudza imfayi.

Dzina la mudzi wa wotisiya

Kodi inali imfa ya mayi kapena ya khanda

- Dziwitsani alangizi a za umoyo (HSA) ngati pachitika imfa ya amayi yodza kamba kauchembere kapena imfa ya khanda



- Yenderani banja limene imfa yachitika, ndikuwafotokozera za ntchito imene mukugwira. Afunseni za tsiku limene anthu ogwira ntchito kuchipatala angazawayendere.

Gwiritsani ntchito mfundo zili koyambilira

(mu gawo louza anthu za ntchitoyi) ngati chokutsogolerani



Zikomo chifukwa chogwira ntchito mwakuzipereka.

Ntchitoyi ikudalira inu amene mukugwira ntchito yodzipereka ku mudzi.

Mavolontiya ngati inu amagwira ntchito yabwino yolumikizitsa anthu akumudzi ndi chipatala.



— VOLUNTEER —



Pamene tichita kalondolondo wa imfa zonse zobwera chifukwa cha uchembere komanso imfa za makanda, zitithandiza kuyetsa kupeza njira zopititsira patsogolo mmene tingathanilane ndi zochitikazi mmakomo mwathu komanso ngakhale achibale.

IMFA YA KHANDA

Imfa ya khanda ndi imfa yomwe yadza pa **masiku 28 oyambilira** a moyo (masabata anayi).



IMFA YODZA NDI UCHEMBERE

Imfa yodza ndi uchembere ndi yomwe mayi wamwalira:

- Pamene **ali yombekezera**
- Pamene **akuchira (kubereka)**
- Patatha **sabata zisanu ndi imodzi** (mwezi ndi theka) chichilire (chibekereni mwana)
- Wapita **padera masabata asanu ndi imodzi** (mwezi ndi theka)

